Transcribed from:

# BWAMPINI

**A. E. Dziko**

**1937 – 2005**

Chichewa (*New Orthography*) Edition **1975**

Bookland International

Kenyatta Drive, Chitawira, Private Bag 140, Blantyre

ISBN 978-99960-13-38-6

by:

**Richard L. Hewitt** and **Neverson Chikusa**

Airwing, Lilongwe

Lammas Day, 2026

https://bwampini.fritillary.org

**Za M'katimu**

Contents

**Mutu**

Chapter

**01** **Dziko la azimu [Azimu]**

The Realm of the Azimu

**02** **Zimeze mfumu ya Angitau**

Zimeze, Paramount Chief of the Angitau

**03** **Mfumu ya a Buwa**

Chief of the Abuwa

**04** **Litsipa ku busa**

Litsipa Goes to Feed the Animals

**05** **Nkhondo**

War

**06** **Bwampini abwerera kwawo – Adutsa mu dziko la Asongo**

Bwampini Returns Home through the Country of the Asongo

**07** **Anyani – Anthu**

Baboon People

**08** **Chikutumbwe**

Chikutumbwe

**09** **Nkhanu yolusa**

A Baleful Crab

**10** **Namatsenga M'Mavuto**

Namatsenga in Trouble

**11** **Namondwe woopsa**

A Terrible Storm

**12** **Gingiswa**

Gingiswa

**13** **Mbalame ibwerera ku Chisa I**

A Bird Flies Back to Its Nest I

**14** **Mbalame ibwerera ku Chisa II**

A Bird Flies Back to Its Nest II

**15** **Mbamba ndi ching'aning'ani [Ching'aning'ani]**

Mbamba and Ching'aning'ani

**Mutu 01**

**Dziko la azimu [Azimu]**

[01.01]

Kudali msonkhano wa dziko lakumwamba, Ku**ntheradi** kumene anthu anzeru zapamwamba anali kukhala. Iwowo kwenikweni sanali anthu, ngakhale adali ndi matupi chifukwa chanzeru zawo zakuya.

[01.02]

Anthuwa dzina lawo lidali **Azimu**. Msonkhanawo adauchititsa ndi mfumu ya **Azimu** onse dzina lake **Tinjiwa**. Iyeyu adali ndi mkazi wake dzina lake **Ngapagwa**. Adali ndi abale ake awiri, **Chimphanza** ndi **Ndomondo**, amenewa kwenikweni adali aphwake.

[01.03]

**Tinjiwa** adabereka ana ake ambiri. Wachisamba adali **Mbamba**, mnyamata wochenjera ndiponso wokonda za chipala. Wachiwiri adali wamkazi, dzina lake **Mziisi**. Ngakhale adali wamkazi, iyeyu adali wamphamvu kwambiri. Mphamvu zake zidaposa mwamuna aliyense.

[01.04]

Wachitatu adali mnyamata wokongola kwambiri dzina lake **Mapiko**. Iyeyu adali ndi thupi lopepuka. Pa zothamanga zokha adalibe mnzake. Popeza **azimu** [**Azimu**] onse adali wotha kuuluka chibadwire, iyenso ankauluka kwambiri moti njiwa siikadapikisana naye.

[01.05]

**Mapiko** adapondana ndi Chang'aning'ani [**Ching'aning'ani**], mtsikana wokongola koyiwalitsa zambiri. Pambuyo pa ameneyu padabadwa chim'nyamata chomvetsa kaso, dzina lake **Chezichezi**. Luso loyimba ndi lopanga zosema lidalidi lakelake. **Chezichezi** adali wodziwa kuyankhula ndi kuchita zanzeru ngati atate ake.

[01.06]

**Azimu** ena ankakwatira koma ena ankangokhala wosakwatira. Koma chifukwa chosachulukitsa pa mtundu wawo, ankakwatirana pachibale. Kotero **Mbamba** adakwatira mlongo wake, **Ching'aning'ani**.

[01.07]

**Chimphanza** adakwatira mdzukulu wake, **Mphukeyi**, mwana wotsiriza wamkulu wake. **Ndomondo** ali ine ndikwatira mdzukulu wangayu, chitsirizira chenicheni cha **Ngapagwa**. Mkazi wakeyo adali **Saisi**. Pa zokwatira zokha, **Azimu** sadasiyane ndi anthu okhala padziko la pansi.

[01.08]

**Tinjiwa** poona kuti dziko lili kum'kulira, abale ake ndi ana ake omwe akhwima nthenga, adaitanitsa chimsonkhano cha **Azimu** onse.

[01.09]

Onsewa atasonkhana m'chinyumba chochezera, iye adadzuka pa chimpando chaulemu. Nthawi yomweyo onse adakhala chete.

[01.10]

‘Mkazi wanga wamphete, aphwanga ndi ana anga onse, kusonkhana kwanu kwandikondweretsa ine, mfumu yanu. Ndati ndikuuzeni chinsinsi cha bambo wanga chimene ndachisunga ngati phukusi la mbewu. Mukulidziwa dziko lino mukukhalali. Tayang’anani pansipo. Dziko ilo likuonekalo mukulidziwa? Nanga pansi pa dziko limene likuonekalo, mukulidziwanso?

[01.11]

‘Bambo wanga adalenga maiko atatuwa: loyamba ndi lino tikukhalali; lachiwiri adalipatsa kwa anthu a pansi, mukuwaonawo; lachitatu, lili pansi penipeni, ndiye kumene ndimatumiza anthu akufa. Ife sitifa, koma apansi okhawo. Dziko lino ndi **Ntheradi**, la anthu amoyo ali pansiwa ndi **Sachokeka**, ndipo la akufawo ndi **Midima**. Monga mukudziwa, chintchito changachi ndi cholemetsadi. Ndimalamula maiko atatu onsewa, ndikupereka zonse zofunika. Lero mwakula aphwanga ndi ana anga ndiye ndati ndikugawireniko udindo wangawu.’

[01.12]

**Chimphanza:**

Akulu, ndikudulani, si chipongwe ayi, mwachita bwino kwambiri.

**Onse:**

Pwa! pwa! pwa! (*m’manja*)

**Tinjiwa:**

Zikomo kwambiri, tsonotu tione wotha kulamula ku **Sachokeka**, nyanja zonse ndi mitunda yomwe.

**Mziisi:**

Bambo akulu a **Ndomondo**, angayesere.

**Ngapagwa:**

Siingawalake ntchito imeneyi, ndiponso ndikuona ngati amalikonda dzikolo makamaka nyanja zake.

**Onse:**

Ha! ha! ha! ha! ha!

**Tinjiwa:**

Mukuti bwanji akulu?

**Ndomondo:**

Ndikamanga nyumba yanga yaufumu mu **nyanja ya mchere** [**Nyanja ya Mchere**], kum'mawa kwa dziko la anthu akuda.

**Onse:**

Pwa! pwa! pwa! (*m'manja*)

**Tinjiwa:**

Nanga ku dziko la anthu akufa?

**Ching'aning'ani:**

Bwanji kupite bambo wamng'ono popeza amakonda kumva chisoni makamaka akamwalira munthu ku **Sachokeka**.

**Mphukei:**

Kodi? Nkwabwino amunanga?

**Tinjiwa:**

Monga mwavomera achimwene?

**Chimphanza:**

Izo ndizo ndimakonda.

[01.13]

Mfumu idapitiriza kuyankhula, kuti pankasoweka mtumiki woyamba wa mithenga. Onse adamvana kuti akhale **Mapiko**, chifukwa ndiye adali wandawala. Kenaka adasankha ogawira luso ndi nzeru anthu a ku **Sachokeka**. Apo sadatsutsane kwambiri, **Chezichezi** adalandira ntchitoyo. Pamene adafika pa mutu wa nkhondo ndiye padali mgwegwe. Mfumu itafunsa, amene adayankha ndi **Mapiko**.

[01.14]

**Mapiko:**

Ntchitoyi ndi yoyenera munthu wamwamuna, akazi ayi. Bwanji atayesa a **Mbamba**?

**Ndomondo:**

Ntchitoyidi ndi ya munthu wamwamuna, koma mukaona amunafe timatupi tathu ndiye ngati tiziwala. Atayesa a chemwaliwa, a **Mziisi**, Tawaonani pamene ayimapa.

**Ngapagwa:**

Apodi ndi zoona sikukondera, koma **Mziisi** akadayesera.

**Mbamba:**

Tisalimbane kwambiri bambo. Ngakhale ali wamkazi, **Mziisi** atha kuyesera.

[01.15]

Pamenepa onse adagwirizana, **Mziisi** adasankhidwa kukhala mtsogoleri wa nkhondo. **Mbamba** adasankhidwa kuti akhale mwini zida ndi chipala. Utatha msonkhano, **Ndomondo** ndi **Saisi**, mkazi wake, adauyamba ulendo wa ku **Sachokeka**. Nayenso **Chimphanza** adapita ku **Midima** ndi mkazi wake.

[01.16]

**Tinjiwa** adakondwa ndikulamula kuti chakudya cha **Azimu** chibwere. **Azimu** amadya uchi ndi chingwa, ndi kumwa manyuchi basi. **Mbamba** ndi **Ching'aning'ani** adamenyetsa zitsulo zawo m'chipala. Anthu a ku **Sachokeka** ndi **Midima** adadodoma ndipo adagwira pakamwa osamvetsa zochitika ku **Ntheradi** pa kumva mabingu.

**Mutu 02**

**Zimeze mfumu ya Angitau**

[02.01]

Ku **Sachokeka**, dziko lachiwiri, kudali bata. Kudali mitundu yambiri ya anthu. **Angitau** ndiwo udali mtundu waukulu wa anthu onse. Dziko lawo lidali pafupi ndi mtsinje wa **Nile** ndipo linkatchedwa **Ngitau**. Mfumu yawo idali **Zimeze**, munthu watsitsi lakuda, wachinyamata, wokhuthala bwino, wamfupi, wansangala kwambiri ndiponso wokongola mwachiufumu.

[02.02]

**Nachimasomaso**, mkazi wake, adalidi munthu wamayi. Iye adali wachifupikire, wonenepa, tsitsi lotuwira, timaso towala, nkhope yosalala ndi yowala ndipo zonse mwa iye zidalidi m'malo mwake. Mwa akazi onse a ku **Sachokeka** panalibe wokongola.

[02.03]

Tsiku lina akucheza ndi mkazi wake, bwenzi lake, ndi nduna ndi mamulumuzana ake mkhonde mwa nyumba yake yokongola yachifumu, adadodoma pomva chimkokomo cha mphepo. Anthu onse adaleka kuyankhula ndi kumayang'anitsitsana. Chimphepocho tsono chidangozungulira nyumba yake.

[02.04]

Mwadzidzidzi adangoona mtambo woyera pafupi ndi nyumba yake. Onse pakhondepo poona mnyamata wamtali, wachilendo, wokongola akuchokera mumtambo, adalenguka ndi mantha ndi kugwa pansi.

[02.05]

'Dzukani musaope.' Liwu lomveka bwino lidatero. Onse adadzuka ndikukhala tcheru. 'Ndine **Mapiko** wamthenga. Ndachoka ku **Ntheradi**, kumene kumakhala **Tinjiwa**, Mfumu ya mafumu kuti ndidzalalike ndi kupereka uthenga wake. Iye wati, kuyambira dzulo maufumu atatu agawidwa, mukuwadziwa kale maufumuwa. Dziko lakumwamba, **Ntheradi**; mfumu yake ndi **Tinjiwa**. Ufumu wa pansi pano, kuno ku **Sachokeka**, uli m'manja mwa **Ndomondo**, mkulu wake. Dziko lapansi penipeni, ku **Midima**, **Chimphanza** ndiye azilamulira.'

[02.06]

'Uthenga wina ndi woti mukafuna nzeru muzipepempha kwa **Chezichezi**. Mukafuna zida za nkhondo, muzipempha kwa **Mbamba**, ndipo ngati ndi koyenera adzakupangirani. **Mziisi** ndiye wodziwa dongosolo lonse la nkhondo.'

[02.07]

Atayankhula choncho, mtambo ujanso udam'phimba. Mfumu idayang'anitsitsa nduna zake ndikufunsa kuti uthenga wa kumwamba aumvetsa bwanji.

[02.08]

‘Tichitenji?’ mfumu idafunsa. Mwa anthu onse omwe adabadwa, nayamwa mawere a munthu wamkazi nalembedwa kuti adzafa tsiku lina, sipanaoneke munthu wochenjera poyankhula ndi kuweruza milandu: ndipo padalibe wodziwa kulewa ndale za anthu, amene akadayankha chifunso chokhwima cha mfumu, koma **Bwampini** yekha.

[02.09]

Iyeyu adali mmodzi mwa nduna zowerengedwa za mfumu. Kwawo kudali ku **Buwa** dziko lomwelo la **Angitau**, koma kafuko kena. Pomva funso loterelo nduna zina zitatu zidaganiza zochitira chipongwe **Azimu**, chifukwa ankafuna kuwalanda ufumu. Ena adati, tingokhala, tione mmene ziyendere.

[02.10]

**Bwampini** yekha adatsutsa nati kwa mfumu ndi kwa makosana onse, ‘Poyamba ife ndife anthu, a ku **Ntheradi** ndi **Azimu**. Ife nzeru zathu zicheperatu poyerekeza ndi zawo. Sitingachite chipongwe, chifukwa mmene tikuyankhulamu akutimva. Mmene agawana maufumu chonchomu ndi bwino, chifukwa ifenso phindu lathu ndi lalikulu. Ndi nzeru zawozo adzatithandiza. Tingochita chaka posonkhanitsa anthu onse kuti amvetsetse. Tikatero tidzakondweretsa **Tinjiwa** poti watitumizira **Ndomondo**, kuti adzakhale wotiweruza pa zinthu zimene sitimvetsa ndi nzeru zathu za umunthu.’

[02.11]

Pomva mawu anzeru oterowo, mfumu, mkazi wake, nduna ndi makosana onse, adamuombera m’manja ndi kumuweramira. Mawu ake adali anzeru. Mfumu adauza nduna yake yaikulu kuti isonkhanitse anthu ake kuti akonzekere za chaka. **Bwampini** atafotokozera chigulu cha anthucho, monga mfumu adapempha, anthu adabalalika. Mmawa mwake, anthu adapha zifuyo monga: nkhuku, nkhosa, mbuzi, ng’ombe ndi nkhumba. Adaphika zakudya zochuluka ndi kukonza zakumwa zoledzeretsa. Anthu onse atasonkhana, mkulu wansembe, **Chipempherere**, adapereka nsembe kwa **Azimu**

onse naperekanso ina yapadera yolandira ndi kuvomereza chitetezo cha **Ndomondo**. Ndipo anthu adadya, navina ndi kumwa kwa ndazioneranji!

**Mutu 03**

**Mfumu ya a Buwa**

[03.01]

Anthu amafanana pa kapangidwe, koma kusiyana kwawo pa zambiri ndi kwakukulu. Kudali mtundu wanzeru, waluntha ndi luso m'dziko lomwelo la **Angitau** dzina lake **Abuwa**. Iwo anali kukhala chakum'mwera m'dziko la mfumu **Zimeze**. Mfumu yawo idali **Bwampini**.

[03.02]

**Bwampini** adali ndi msinkhu wautali, wokulupala, wa tsitsi lobiriwira, nkhope yake idali yaifupi, phuno yake yaitali ndipo kunsonga kwake idali ngati mlomo wa chiombankhanga. Adalidi wokongola m'maonekedwe.

[03.03]

Akuluakulu amtundu waChi**buwa** ankati **Bwampini** akadali mnyamata, atsikana ankangomulondalonda, nkhalamba ndi tchembere zomwe zidamfunsirafunsira. Chachikulu kopambana, iye adapambana anthu anzake onse pa nzeru. Anthu ambiri poganiza ankati, pang'onong'ono bwenzi atakhala mwana wa **Tinjiwa**. Poyankhula zanzeru kapena mtsutso ndi anzake, pogamula milandu, pa masewera a mitundu yonse, padalibe mnzake.

[03.04]

Chifukwa cha zonzesi, **Zimeze** sadapeneke kumusankha iyeyu kukhala mulumuzana wamkulu mwa onse ndiponso nduna yake. Mwa chiganizo cha anthu ndi **Azimu** okhala

ku **Ntheradi**, iye adachita mwayi wokhala ndi mkazi wolingana naye pafupifupi zonse. Dzina lake adali **Namasinkho**. Munthu ukakhala wanzeru, tsoka ilo mwina umakwatira chidzete, kukhala wotsetekeka, mkazako mwina amakhala kaphulika; Khungu!

[03.05]

Phula lotereli **Bwampini** adalibe. Adagwiradi pakatikati. Awiriwa adakondonadi; chikondi cha bulangeti! Mtendere udali wathunthu pakati pawo. Anthu odzawayendera sadaleke kuzizwa ndi udongo, ufulu ndi kumvana kotereko.

**Mutu 04**

**Litsipa ku busa**

[04.01]

Ku **Ntheradi** kudali chimwemwe cha malipenga; nako ku **Sachokeka** kudali ufulu wokhawokha. **Zimeze** ndi anthu ake sadaleke kuthokoza **Ndomondo** chifukwa zonse zidayenda mwakaso.

[04.02]

Ngakhale kudali chimwemwe chotere, m'dera lina, kumene kudali anthu amtundu wina, nawonso anthu aluso (koma pang'ono), sadali osangalala kwenikweni. Kwenikweniso mtunduwu udali wopanda nsangala wofuna kutsutsulatsutsula ena pachilonda.

[04.03]

Mtunduwu unkatchedwa **Agangire**. Mfumu yawo idali **Gangire** amene. Mfumuyi idali yokalamba koma yanzeru. Munthutu akakalamba nthawi zina amatayirira pa zinthu zina. Ana ake ndiye ankangokhala ngati alowa kale ufumu.

[04.04]

**Gangire** adali ndi ana ake aamuna awiri, **Litsipa** ndi **Utwa**. Woyamba ndiye adali wamkulupo. Iyeyo ankakonda kumuwetetsa ng'ombe ndi zifuyo zina. Wang'onoyo, **Utwa**, popeza kuti adali ngati chitsirizira, ankakhala kumudzi kusangalatsa ukalamba wa atate ake. Komatu adali ndi mphamvu zambiri.

[04.05]

Tsiku lina **Litsipa** atapita ku ubusa, iye mbuzi zake adangozisiya pa msipu wambiri. Iye adafuna mthunzi pena, nakhala pansi. Akudzikhalira choncho akuganiza zake, chinthu china chidamudabwitsa; kudalibe mitambo konse, koma mwadzidzidzi, padaoneka mitambo itatu yoyera, chakum'mawa, youluka ndi liwiro. Posakhalitsa adayionera chapafupi. Kenaka adangoona kuti ndi anthu, atatu aimirira pafupi naye: anthu ovala zonyezimira ngati dzuwa, nkhope ngati makanda, okongola kosasimbika.

[04.06]

Iye mwaulemu adawalonjera, natonthola ndikuwayang'anitsitsa mosachita mantha. Iye adamvetsa kuti adali **Azimu**. Mosataya nthawi, **Ching'aning'ani** mkazi wa **Mbamba** adayankhula.

[04.07]

**Ching'aning'ani:**

Kodi ukudabwa? Ife tadza kudzakuchezetsa, kwina takukonda ndipo tabwera ndi mphatso. Utchule ndani mwa ife ali wokongola. Ameneyo ndiyemwe ati akupatse mphatsoyo.

**Mziisi:**

Komatu pamenepa uyunera kuganiza bwino.  Ukatchula ine ndikupatsa mphamvu zopambana aliyense amene amamwa madzi.

**Chezichezi:**

Ine ndidzakupatsa luso loyimba mngoli, kusemasema ndi kujambula. Mwini wa zopangapanga zonse udzakhala iwe.

**Ching'aning'ani:**

Ukanditchula ine, udzakwatira mkazi amene ali wokongola mwa atsikana onse a ana a anthu.

[04.08]

Pamenepo mwana wa mnyamata adavutika ndi maganizo. Zimenezi sizinali zakutulo koma zoonadi. Mphamvu adali nazo, koma mpang'ono; ana anzake adamukanika kale, lero adali ndi mwayi wopeza mphamvu zowonjezera zomenyera! Ndiponso tsopano ndi akuluakulu omwe sadzamuopsanso. Kwinaku adasirira zoyimba ndi zopangapanga. Iye mwana wa mfumu akadatha kuvinitsa ndi akambuku omwe tsopano ndi nyimbo zake zotsekemera. Atate ake, akadawapangira mipando, matebulo, ndi mabedi omwe. **Litsipa** mbiri yake ikadamveka ponse.

[04.09]

Koma ganizo la mtsikana wokongola koposa azimayi ndi atsikana onse apansi pano lidamkondweretsa kwambiri. Sadatayenso nthawi posankha, adaweremira **Ching'aning'ani**. Namutchula mfumu ya anthu okongola onse. **Azimu** nthawi yomweyo sadachedwenso, **Ching'aning'ani** yekha adatsalira namfotokozera bwino za mtsikanayo. Dzina lake **Namadanitsa**. Adali kukhala ku dziko la **Angitau** ndi **Ndaziona**, mng'ono wake wa **Zimeze**.

**Mutu 05**

**Nkhondo**

[05.01]

Zinthu zonse zimayenda monga momwe adazipangira. Zonse zimayamba ndi kutha. Munthu akababwa amangochita zomwe adamulembera, kaya ndi tsoka kaya ndi mwayi, zonsezo amangokumana nazo, azifune kaya asazifune, mmomwemo. **Namadanitsa** ali ku madzi kukachapa ndi anamwali ake, adaona chinthu choyenda pamadzi chikubwera. Pochiyang'anitsitsa adaona kuti ndi ngalawa yaikulu. Atayang'anitsitsabe adaona kuti mudali anyamata ndi anthu akuluakulu.

[05.02]

Ngalawa itakocheza pa gombe, mkulu wa onse adatuluka ndi za nkhondo, nafunsa ngati atsikanawo adali kudziwa kumene kunali kukhala mfumu ina, **Ndaziona**, mphwake wa **Zimeze**, mfumu ya **Angitau**. Pamenepo **Namadanitsa** adadzuka ndikuyamba kumulonjera mlendoyo ndi anzake ena onse. Kenaka adafotokoza kuti, **Ndaziona** adali kukhala kumtunda kwenikweni kwa **Nile**, pafupi ndi **Nyanja**; **Zimeze** mkulu wake anali kukhala cham'munsi mwake. **Namadanitsa** adapitiriza kufotokoza kuti, 'Pamene mwaimapo ndi pafupifupi ndi nyumba ya mfumu, imene simungaione chifukwa yabisika ndi mitengoyi. Mukafuna kukaona mfumuyo, ine mkazi wake, **Namadanitsa** ndikuperekezani ngati palibe choletsa.'

[05.03]

Pomvadzina la **Namadanitsa**, **Litsipa** adathunthumira ndi chimwemwe, nanyivula pang'ono nati: 'Poti ndaona kumeneko kukhala ngati nkopitika ndi ngalawayi, talowani mom'muno ndi alezi anuwa, kuti tifulumire, chifukwa tikufuna tiyende mwamsanga.' Mwamsangamsanga adanong'oneza mmalinyero wamkulu kuti asapitenso kunyumba kwawo.

[05.04]

Chosadziwa, mtsikana mmodzi sadalowe nawo adangobisala. Poona kuti ngalawa ikuthamanga pamadzi ulendo wa kwawo, mtsikana uja adakuwa ndi kulira mokweza ngati lipenga. Anthu adabwera kudzaona, koma adapeza **Litsipa** atapita kale, ali pafupinso kufika kwawo, **Agangire** poyendetsa ngalawa adali opambana.

[05.05]

‘Amayi, a **Namadanitsa**, abedwa ndi **Agangire**!’ adatero pouza anthu onse.

[05.06]

**Ndaziona** atamva zimenezo, zidamzula moyo! Sadathe kulira kapena kuyankhula. Atapeza nzeru, adasonkhanitsa anthu ake, nawafotokozera kuti mwa zolengedwa zonse, iye, **Ndaziona**, adalibe mnzake. Kameneka kadali kachiwiri kupeza milandu yotere, sabata yatha mwana wake wachisamba adampeza mikango itaphangirana. Kodi zimenezi zidali zotani?

[05.07]

Adatuma anthu asanu pa hatchi kukauza mkulu wake **Zimeze**, ndi kumdziwitsa kuti **Gangire** wamema nkhondo ya **Angitau** pomubera mkazi wake **Namadanitsa**. Iye yemwe adauza amisiri okonza ngalawa kuti akonzeke, adauzanso mulumuzana wake wa nkhondo kuti asonkhanitse anyamata amagazi ndi kuwapatsa zida za nkhondo. Mkulu wakenso atamva adachita chimodzimodzi. Posakhalitsa adatulukira ndi ngalawa zake za nkhondo.

[05.08]

**Gangire** wamkulu atamva zimene mwana wake adachitira **Zimeze**, pomubera mlamu wake, adadziwiratu kuti nkhondo ikubwera, adauza **Kazione**, mkulu wa nkhondo kuti akonzeke, chifukwa padalibenso chibwana.

[05.09]

Tsiku loti mawa ndi nkhondo anthu amaso, adaona kumwamba mbalame zikuluzikulu zikumenyana ndi kusosolana nthenga. **Mbamba** adayimba malipenga ake ndi kumenya

ng’oma zake ‘Gulugulu!’ **Sachokeka** adadzadza ndi mabingu ndi zing’aning’ani. Kudziko la **Agangire** kudali bwalo lobulika bwino, lomwe pamachitikira masewera a mitundumitundu. Kalekale makolo omwe adaponyerapo nkhondo adafika ndi kudzadza.

[05.10]

Ku **Ntheradi**, **Tinjiwa** ndi anthu ake adagawikana, ena adafuna kuthandiza **Angitau** ena **Agangire**. Mitima ya anthu onse idagunda mopitiriza, nthumanzi idagwira aliyense.

[05.11]

**Bwampini**, Kazembe wamkulu wa **Angitau** onse ali pa hatchi, adatsogolera ankhondo onse a **Angitau**. **Kazione** naye adachita chimodzimodzi.

[05.12]

Maliro, zilonda, kulira, njala, nkhawa zidazadza ponseponse pa dziko la **Sachokeka**. Phokoso la mikondo, zibonga, mauta ndi nyankhwa zidagonthetsa makutu a anthu. **Pherera**, Kazembe wachiwiri wa **Chingitau** adasakaza **Agangire** kwabasi. Kumangowapha ngati adzowe. Iye chibadwire chake, mpeni, mkondo, muvi sizidathe kulowa m’chikopa chake. Chifukwa cha ichi adangopita dala pakati pa amaliwongo, omwe amamponyera mipeni, mikondo, mivi, koma osabaidwa. Naye **Kazione**, amene adali mwana wa **Ching’aning’ani**, chifukwa atate ake, **Chokhola**, amene adagona ndi **Mzimu**wu tsiku lina, ngakhale adali mkazi wamwini, nayenso adasakaza **Angitau**.

[05.13]

**Utwa**, mwana wamng’ono wa **Gangire**, nayenso adapambana koopsa. Munthu wamtali, wathupi, wodziwa kulewa ndi kuponya, adachitadi zachimuna.

[05.14]

Mitembo ya anthu akufa pambali zonse idakanika kukwiriridwa. Afisi ndi nyama zankhuli zonse zidachitadi chaka, mbalame zolusa monga ngwangwa, zidapeza chajira. Zimeze adavutika m'moyo poona mwana wa mchemwali wake **Saopa**, atabaidwa m'mimba ndi mkondo wa **Kazione**. Adaponya mivi ingapo kuti alase mdaniyo koma mivi inkangodya dothi; ina idalasa **Agangire** ena. **Saopa** adafa adakali mbeta yachimuna (akadali m'bwalo).

[05.15]

**Pherera** atalusa kwambiri, adathamanga pakati pa **Agangire**. Poona maponyedwe ake, osaphonya ndi osapherereka, ankhondo adamwazika. Poona zimenezo, **Utwa** adadzipereka nafuna kumenyana mikondo yokhayokha iye ndi **Pherera**. Pamenepo pakadakhala ngozi! **Pherera**, amene chida chilichonse sankaopsedwa nacho, adamgudukira mnzakeyo ndi kumponyera mkondo. Nthawi yomweyo padagwa mdima, mkondowo udamenya chikopa cha **Ching'aning'ani** amene adafuna kupulumutsa **Utwa**. Chifukwa cha mphamvu za **Pherera**, mkondowo udakalowa m'matumbo nutulukira. Komabe **Utwa** adagwa ndi mpemera, osabayidwa chifukwa cha **Ching'aning'ani**. Malipenga adalira, chifukwa kudali kutada. Anthu onse ankhondo adapita kuzithando zawo. Nthawi ya usiku adapeza nthawi yoyikira maliro ndi kupereka nsembe kwa akufa. Kutacha, mitima idada nkhawa bi.

[05.16]

Ankhondo adakumananso, 'Kho! Kho! Thwe! Thwe! Mayo!' Phokoso lidamvekanso ponseponse. **Bwampini** ndi nzeru zake zopambana adaonetsa kukula kwa umisiri wake wa nkhondo. Atapangana ndi **Pherera**, kubwalo la nkhondo kudapita anthu ochepa **Achingitau**. Pompo **Utwa** ndi **Kazione** adapusitsidwa, naganiza kuti **Angitau** kugonja kwawo kudali tsikulo, osatinso lina.

[05.17]

Koma iwowo sadamudziwe **Bwampini**. Iye adapanga chihatchi chake chosema, chachikulu. Ankhondo ambiri adalowa mmenemo, ulendo wa **Zimeze**, **Ndaziona**, **Chamuna** ndi ankhondo ena onse otchuka. Ankhondo ena adachiyendetsa chihatchi

chija pakati pa usiku mpaka pafupi ndi chipata chamzinda waukulu wa **Gangire** – **Huwa**. Podzuka **Agangire** adapeza chihatchi chokongola, chosema, nazizwa nacho kwambiri. Akazi, ana, nkhalamba ndi amuna onse odwala amene adakhala kunkhondo adachiyang'anitsitsa kwabasi ndi kuchita nacho chidwi. Adachikankha nachilowetsa mumzinda wawo. Naganiza kuti mwina iyi ndi mphatso yachipepeso yochokera kwa **Angitau**.

[05.18]

**Namadanitsa** nayenso adabwera, nachiyang'anitsitsa. Atachiona iye adauza **Agangire** kuti mudali anthu m'katimo, koma adamutsutsa, namseka. Iye adayesetsa kuyankhula zambiri zofuna kuseketsa am'katimo koma adalephera. **Agangire** atachiyang'anitsitsa chinthu chachilendocho ndi kutopa nacho, adachoka ndi kupita kwawo.

[05.19]

Usiku, anthu onse atachoka nakagona, **Bwampini** adauza ankhondo aja kuti atuluke. Onse adataluka ndikumenya nkhondo yakabisalira mpaka kutsegula zipata za mzinda. Ankhondo ena a **Chingitau** adalowa natentha **Huwa**, nagwira mfumu **Gangire**; napha amuna onse mumzinda ndi nkhalamba zomwe, koma atsikana ndi tchembere zachitsikana zidatengedwa. **Utwa** ndi **Kazione** adadodoma ndi umambala wa **Bwampini**, adangodzipereka, ndipo nkhondo idathera pompo. Awiriwa sadaphedwe.

[05.20]

**Zimeze**, atatenga chuma cha **Huwa** ndi atsikana omwe, adalamula ankhondo ake kuti asonkhane. Adachita chaka choti agonjetsa **Gangire**, napereka nsembe zothokoza **Azimu**, makamaka **Mziisi** [**Ndomondo**], amene adathandizadi kopambana kulira akufa. Kenaka adalamula ulendo wobwerera ku nyumba. Anthu obwerera kunyumba adali ochepa. Mwa ngalawa makumi asanu zomwe zidabwerera, makumi atatu adadzaza ndi anthu amoyo, chuma cha **Huwa** ndi atsikana **Achigangire**.

**Mutu 06**

**Bwampini abwerera kwawo – Adutsa mu dziko la Asongo**

[06.01]

Kaya ndi tsoka, **Bwampini** adalawirana ndi mfumu **Zimeze**, namuuza kuti iye adzera njira ina pobwerera kwawo. Adatenga ngalawa zisanu, muli monse mudali anthu khumi. Iye, m'malo moyenda chodutsa **nyanja** [**Nyanja**] adafuna kutalikitsa, pomamka nayo mulitali mwake. Zakudya adali nazo zambiri. Madzi adali nawonso ambiri. Vinyo wotsekemera ndi wowawa adali nayenso. Sadasowe kanthu. Masewero amitundumitundu adali nawonso. Anthu a pangalawa onse adali ndi nsangala. Ankakamba za ku **Gangire**, nzeru zotamandika za **Bwampini**. Chifundonso chidawafikira nayamba kukamba za kwawo, ana ndi akazi awo, ndi onse achinansi. Nkhani sizinawasowe. Akupalasa ngalawa, adaona pa gombe pena mitengo yobzalidwa bwino ya zipatso za mtundu wa malalanje, ndipo zipatsozo zinali zakupsa ndithu. Pompo amalinyerowo adakamba ndi **Bwampini** zakukaona malowo, ngati nkotheka, kuti akapemphe nawo zipatsozo.

[06.02]

**Bwampini**yo sadawakanize. Adakocheza ngalawa pagombe, natuluka. Poyang'anitsitsa, adaona kuti dzikolo linali ngati lopanda mwini. Osusukawo adathamangira kumitengoko kukathyola zipatso. Ena adatsalira m'ngalawa, enanso adali panjira yaku zipatso.

[06.03]

Pasanapite nthawi adamva kulira uku ndi uku, poti ayang'anitsitse adaona njoka zikuluzikulu, zangoyimirira pansonga za mitengo, zikumvetsera ndi kuyang'anitsitsa. Njoka zina zinali kuthamangitsa ena, zina zinali kugogoda enanso. 'Taonani!' adafuula ena onse amene adatsalira m'ngalawa. Pamenepo padali liwiro, zina zikuluma, zina zikuphedwa. Pafupifupi anthu asanu adalumidwa, mmodzi mwa olumidwawo adali **Chimadyo**, wamadyo abasi.

[06.04]

**Bwampini** yekha ndiye adachita chamuna. Ikumpitikitsa njoka, adaima nayitseteka mutu. Apa padalinso nkhondo. Njoka zina zidamuthamangira malilime ali pamtunda. Mwakuchenjera kwake njoka ili yonse yobwera idasengedwa. Anthu oonera adangoona manja a **Bwampini** akuzugulira ngati mkombero, kupha zilombo. Adapha khumi zokha! Njoka zina poona zinzawo zili lambalamba, zidathawira kumphako zawo m'mitengo. Mwamsangamsanga **Bwampini** adathamangira ku ngalawa, ali olefuka. Ulendo udayambikanso.

**Mutu 07**

**Anyani – Anthu**

[07.01]

Onjenjemera ndi achisoni, amalinyero adayenda ulendo wawo, poganiza za njoka zimene adaziona, ndi chakudya chomwe sadachifune. Poganiza za anzawo amene adafa chifukwa cha kulumidwa ndi asongo olusa aja, chisoni chawo chidakulirakulira.

[07.02]

**Bwampini** nayenso sadathe kukondwa kwenikweni poganizanso za zimenezi. Koma poganiza kuti kukwiya kulibe phindu ndi bwino kumva chisoni, koma osapitiriza. Iye adagwira mngoli wake, nayamba kuyimba nyimbo zatsekatseka [zatseketseke] zoiwalitsa mavuto, zopha chisoni. Adaitanitsa vinyo ndi chakudya chokoma. Amalinyero adadya ndi kuvina. Onse chisoni chidamwazika.

[07.03]

Ulendo uli m'kati; adaona pena pakuyaka moto. **Bwampini** anachita chidwi ndipo adaganiza zokazondanso malowo. Kwina adafuna kukatunga madzi abwino popeza madzi amene ankamwa adali atakhalitsa, kwa chaka chathunthu.

[07.04]

Ngalawa zidakochezanso pagombe. Onse adatuluka, nafuna kuyenda pang’ono pamtunda. Ena adafuna kukhala pansi ndi kumacheza, ena adafuna kuyendera dziko. **Bwampini** adafunafuna chitsime choti n’kutungapo madzi. Adachipeza alikuyenda ndi amalinyero awiri. Padali mtengo wautali pafupi ndi chitsime. Mmene mmalinyero wina adati nditayang’ana cha m’mwambamu, adangoona chimunthu cha bweya thupi lonse. Poti, ‘Hi! nchiyani?’ Chimunthucho chidamkoweratu ngati ngowe. Adalira, ‘Mayo!’ Chidamthyola khosi ndi kumkanyanga. **Bwampini** poti ayang’ane, adangomvanso mmalinyero winayo, ‘Mayo!’ Chamthyolanso kale khosi, waka! Pamenepo tsono ndiye padali nkhondo.

[07.05]

Chilombo chija poti chikowe **Bwampini**, chidangomva manjawa ngwanju! Nachonso chidalira chakwawo. Chidakalipa ndi kunola mano. Chidatsakamuka m’mwamba kuti chidzangomgwinya. **Bwampini** adachitseteka mutu. Pamenepo chidalira chimunthu kuti, ‘Mayo!’ Kenaka khu! Nthawi imeneyi amalinyero ena amene amangoyenda, nawonso adakumana ndi chikhamu cha anyani.

[07.06]

Anyaniwo adali ngati anthu koma adali ndi mano a chinyama. Kunamveka kulira **anyani-anthu** [**Anyani-anthu**] akumenyana ndi anthu enieni. Padali chinkhondodi. Anyaniwa adathyola nthambi. Adali ndi miyala ndi ndodo, zonsezo ankaponya, mwina kulunjikadi. Koma anthu ndi anthu, **Bwampini** yekha ndi mkondo wake ndi mivi adapha anyani makumi anayi. Amalinyero enanso adapha awo anyani. Anyani adapululuka pafupi onse kutha, ena adachita chothawa. Nkhondo itatha onse adathamangira ku ngalawa; posakhalitsa nkhafi zidamenyeka.

**Mutu 08**

**Chikutumbwe**

[08.01]

Maganizo adapha **Bwampini**. Adaganiza za mzinda wa **Huwa**. Adalingaliranso za bwenzi lake, **Pherera**, za mfumu **Zimeze**, za nkhondo ya **Angitau** ndi **Agangire**. Mtima sunali m'malo.

[08.02]

Nawonso amalinyero mitima idasweka polingalira za anzawo amene adaphedwa ndi **anyani-anthu** [**Anyani-anthu**]. Podziwa nyimbo zokoma ndiye tsache lake la chisoni ndi maganizo ena onse oipa ndi aupandu, adauza mmisiri wa nyimbo [**Muvina**]. Iye adayimba zachisoni cha **Azimu**, za chikwati cha **Bwampini** ndi **Namasinkho**, nkhondo ya **Angitau** ndi **Agangire**, natsirizira nyimbo ya chikwati cha **Tinjiwa** ndi **Ngapagwa**. Nyimbo zidali zotsekemera kopambanadi. Onse mitima yawo idasangalala ndi kuzizira. Makamaka **Bwampini** pamene adamva nyimbo ya chikwati chake ndi **Namasinkho**.

[08.03]

Ulendo uli m'kati, kulira kwa mbuzi ndi nkhosa pa kachilumba kena kudamveka, 'Me-me-me-me-be-be-be!' Kulira kotereku kudawakumbutsa nyama ya mbuzi ndi nkhosa. Nkhuli idagwira aliyense wa iwo. Ndi kale lija limene adalawa nyama yophika ndi yootcha yomwe.

[08.04]

**Bwampini** chilakolako chokasuzumira sadachipirire. Koma ulendo uwu adachenjera. Adasankhula anthu khumi ndi awiri. Ena adawauza kuti abadikira chifukwa mwina kumene anali kupitako kudali zoopsa kwambiri, tsono kudali bwino kuti ena apulumekeko.

[08.05]

Apo adamvera. Atakocheza ngalawa anthu osankhidwa adayamba ulendo wawo. Adayendayenda osaona kanthu, kenaka atayenda pang'ono, adapeza phanga. Poti asuzumire m'katimo, adaona nkhuni, moto ndi nyama yambiri ya nkhosa ndi ya mbuzi.

[08.06]

**Bwampini** atachita odi, sadamve liwu ndi limodzi lomwe. Onse adangolowa. Popeza njala idawapota, aliyense adadula nyama kuti awotche monga akadathera. Atadya adamwera vinyo yemwe adabwera naye. Akucheza, adamva phokoso la nkhosa ndi mbuzi zomwe, zikubwera. 'Me-me-me; bere-re!' Lowulowu zonse zidalowa, koma mbusa wawo osamuona. Zidali nkhosa ndi mbuzitu, ndiye ngati ng'ombe kukula kwake. Posakhalitsa adamva kutsokomola, kenaka mwini wake watulukira. Mwini wakeyo sadamwazemwaze maso ayi. Adangofika kugwetsa mtolo wake wa nkhuni, kenaka nkutseka pakhomo ndi chithanthwe.

[08.07]

**Bwampini** adamuyang'ana, onse adamuyang'ana. Koma ee! Amuna! Onse adanjenjemera ndi mantha. Chimwendo uko, diso limodzi lokha pamphumi, ali thobothobo kutalika! Chimenechi chidali **Chikutumbwe**.

[08.08]

Mmene adacheuka ndikuyang'anitsitsa adangoona tianthu tatsamiranatsamirana. Ndiye icho chidasekerera nachifunsa [nafunsa, nawafunsa], 'Ndinu yani?'

'Ndife **Angitau**.' **Bwampini** adayankhula. Mochenjera.

'Ndiwe yani ukuyankhulawe?'

'Ndine Ndingolira.'

[08.09]

Mwamsangamsanga chidagwira anthu awiri miyendo yawo, ndikuwamenyetsa pamodzi mitu yokhayokhayi.

[08.10]

Nthawi yomweyo kuwaponyeratu m'kamwa mmodzimmodzi, n'kumeza gwidyo! gwidyo!

[08.11]

Pamenepa amalinyero adasisima ndi mantha. Chimdani chawocho chidatenga ndowa zitatu za mkaka zodzadza, ndi kutsitsira (kumwera). Chitatero chidagona. Kutacha chidagwiranso anthu awiri kuwamenyetsa mituyi, kuthanthweko, kenaka n'kuwatafuna. Kenaka n'kutsitsiranso ndi ndowa ziwiri zodzadza ndi mkaka wophika.

[08.12]

Chitatuluka, **Bwampini** adaomba m'manja ndikugwedeza mutu. Ataona chimtengo chachikulu adachisongola bwino kunsonga, nawauza anzake kuti usiku akhale tcheru. Kukuda kudamvekanso, 'Me-me-me; berere… berere re re.' Chilombocho chidatulukira. Chidatseka pakhomo, nichigwira anthu awiri ndikuwakulumunya ngati siwiti, sichidawatafune.

[08.13]

**Bwampini** adanyamuka nachifunsa nati, 'Kodi mudamulawa vinyo wotsekemera?'

'Tangofulumira naye, iwe!' chadayankha [chidayankha]. Chitalawa vinyoyo **Chikutumbwe** chidabwekera, ndi kupemphanso wina. Kenaka dzandidzandi, kuledzera. 'Iwe ndidzakudya potsiriza, chifukwa ndiwe waulemu ndi womvera.' Mosachedwa **Bwampini** adatenga chimtengo chosongola chija nachiika pamoto, chitafiira, adauza anzake kuti athandizane kubaya diso la **Chikutumbwe**cho.

[08.14]

Sadachedwe, adachinyamula chimtengocho ndi kuchiponya ndi nyonga m'diso la chilombocho, mpaka thudzu, kuthudzuka! Apo chidafuula ndi kubuula. Anzake onse adabwera.

'Ukuliranji?'

'Akundipha kuno Ndingolira.'

'Ndingolira?' anzakewo adafunsa. 'Tsono poti ukungolira, balira!'

[08.15]

Kutacha **Bwampini** ndi anzake adadzimangirira kumimba kwa nkhosa. Zikutuluka, **Chikutumbwe** chidayesayesa kufufuza koma sichidapeze kanthu. Munthu wakhungu! Panja anthu aja adadzimasula ndi kuthawa. Adauyambanso ulendo ndipo ali m'kati mwa **nyanja** [**Nyanja**] **Bwampini** adafuula, 'Tsalatsala iwe!' **Chikutumbwe** chidatola chimwala, chithanthwe, nichiponya ndi mphamvu zake zonse powawidwa mtima kuti chanyengedwa. Pang'onong'ono onse adakafa! Chimwala chidagwera pafupi ndi ngalawa, ndipo pang'onong'ono ngalawazo zikadatembenuzika.

'Ukumana ndi bambo wanga m'madzimo sakusiyani.' **Chikutumbwe**cho chidafuula.

[08.16]

Ulendo udali pakati koma ndi chisoni.

**Mutu 09**

**Nkhanu yolusa**

[09.01]

Misozi onse idayenderera m'maso ofiira, nkhope zakugwa, chakudya sichinathe kulowa pakamwa, poganizanso kuti anzawo ena afa. Kujiwa ndi chilombo cha m'tchire adakamvetsa koma munthu mnzawo!

[09.02]

**Bwampini** adadziwa kuti ulendo wawo adali nawo tsoka lalikulukuludi. Anthu pafupi makumi awiri adafa, ena ndi anyani, ena ndi njoka, koma otsirizawa adachita kudyedwa ndi munthu. Munthu wanzeru zake ndi kusataya mtima angakumane ndi zovuta za mtundu wanji.

[09.03]

**Bwampini**, modzikakamiza adayesetsa kuoneka wokondwa, nawapempha kuti avine. Adayesetsa kukondweretsa anthuwa ndi nyimbo zake za nthetemya, zomvetsa kaso. Pomva kuzuna kwa nyimbozo, misozi idauma nayambanso kukondwa onse. Ali kuyendabe choncho, chimwemwe ndi nyimbo zili m'kati, poti apenye, wina adachita ngati akuona mafunde akuluakulu kutsogolo ndithu, komatu tsono kudali bata. **Bwampini** naye poti ayang'ane, adaona kuti madzi anali kuponyedwa m'mwamba ndiponso ankachititsa timitambo kumwamba.

[09.04]

Nthumazi idamgwira. Adawauza onse kukhala mmalo mwawo, ndi kugwiritsa zida zawo chifukwa kutsogoloko kudali chinthu china chofuna kuwaopsa. Onse adamvetsa. Tsono zidatsala ngalawa ziwiri zokha. Koma onse adali mu imodzi, chifukwa chochepa anthu, ndipo ina amachita kukoka, mudali zakudya, Akuti aziyandikira adaona madzi akungochita ngati kuthamanga, ndiponso ngalawa kuyenda kwake kudali kopendekeka. Sadaone chinthu chodabwitsa chilichonse koma madzi ankangowazidwa m'mwamba. Mmene amapita cham'kati ndithu mwa madzi, adangoona chinthu cha miyendo khumi ndi iwiri chitaimirira pamadzi.

[09.05]

Mitima myuu! Mantha adawagwira kwambiri. Woyendetsa adachita ngati sakuona namapita molambalala; akuti adutse, zachisoni, tsitsi lonse chiliri.

[09.06]

Nthawi yomweyo chidagwira anthu asanu ndi mmodzi ndi kuwamiziratu. Sichidaonekenso. Ngalawa idayenda ndi liwiro pamenepo. Kudali kulira kwenikweni; kokuwa... maliro. Onse adachita mantha, ndi **Bwampini** yemwe adanjenjemera. Kuti onse adapulumukawo akafika kumudzi zidali zokayikitsa kwabasi. Anthu asanu ndi mmodzi nthawi imodzi kupitiratu, akuona ndimaso.

[09.07]

**Bwampin**i adadzitonthoza ndi kutonthoza anzake pakuwakumbutsa za kwawo, nkhondo ya **Angitau** ndi **Agangire**. **Muvina** adagwira mngoli wake nayimba nyimbo zotsekemera kopambana, zovomerezana ndi zimene adanena **Bwampini**.

[09.08]

Onse mitima idayamba kuzizira, napukuta misozi. Vinyo wafungo ndi wotsekemera adabwera. Chakudya chophikidwa bwino ndi mafuta chidabwera.

[09.09]

Kudali kuvina, kuyimba, ndi kumwa tsikulo, kuchita ngati kutsendera pansi zonse zimene zidachitika. Akuyendabe ndi kukondwa choncho, adaona kagombe kokoma, kamchenga, dziko lopatsa nsangala. Onse adasirira kuponda mtunda ndi kuthamanga pang’ono. Kungokhala pansi, kusasitsa miyendo. **Bwampini** naye adafuna kukaonanso dzikolo. Munthu wanzeru saleka kuonetsetsa kuti aphunzirepo kanthu kenakake.

**Mutu 10**

**Namatsenga M'Mavuto**

[10.01]

Pofika pagombe adapeza zambiri zochititsa chidwi; msipu ndi tizomera tabwino ndi tokongola. Mbalame zazikulu ndi zazing'ono; tinyama tina tongoyenda ndi tokwawa.

[10.02]

**Bwampini** adauza anzake kuti amudikire, iye adapita pa kaphiri kena ndi mivi yake, atafika paphiripo adaona kwina kukufuka utsi, koma nyumba yokha osaoneka. Adasirira kwambiri kukaonanso ndani adali mwini wa dziko lokongola lachoncholo. Atayang'ana ndi kuyang'anitsitsa ndithu, adafuna kubwerera kwa anzake. Akuti azipita, adaona mphoyo ikuderuka, iye adamyata bwino. Adaiwenda, kenaka kuikokera muvi umodzi. Umodzi ndi umodzi idagweratu pansi. Muvi udatulukiranso, nukagwera poteropo. Iye adathamanga nakainyamula. Atafika nayo kwa anzakeko adaisenda. Kudalidi phwando. Nyama ina adachita yowotcha, ina yophika. Vinyo wonunkhira ndiponso wokoma amene adabwera naye **Muvina**, adamwa kuti atsitsire.

[10.03]

Atadya adawafotokozera anzakewo zimene adaona. Adaona utsi. Kudali kofunika kuti akaone kudali ndani kumeneko. Atatsutsanatsutsana adamvana kuti agawane magulu awiri; lina anthu khumi ndi asanu, lina chimodzimodzi. Adaombeza ula kuti apite ndani. **Muvina** ndi gulu lake udawagwera, tsono sadataye nthawi, koma kuuyamba ulendo nkumapita. Aulendo adatenga nthawi kukafika chifukwa kumene adali kupita kudali kutali ndithu. Atayenda pang'ono adaona nyumba yokoma, yaikulu yokhala ndi chimuni (chitulutsira utsi). Poyang'anitsitsa pabwalo, adapeza kapinga wabwino ndi maluwa ambiri okongola kwabasi.

[10.04]

Akadachita chidwi choncho, adadzidzimuka poona mikango, akambuku, afisi ndi nkhumba. Adafuna kuthawa, koma **Muvina** adalimbitsa anzake mitima. Chodabwitsa chidali cha kuti nyamazo sizidachite ukali koma zidasendeza mofatsa. Zidawagwedezera michira, zina zidawanyambita. Iwo adazizwa ndi nyama zofatsa chonchi. Chidwi chisanawathere, adamva nyimbo zokoma kwabasi m'kati mwa nyumba, nthawi yomweyo mitima idali pha-pha-pha. Adamvetsa tsono kuti mwini wa zonse adali kugwira ntchito ya mtundu wina mnyumba yake. Iwo onse poti njala idawapola kwabasi, pochitanso chidwi ndi nyimbo zokoma zomvekera m'kati, adafunitsitsa kulowa m'nyumba mwa munthu wosadziwikayo.

[10.05]

**Muvina** adavomereza kuti alowe, koma iye adatsalira pambuyo dala. Onse atalowa iye adabisala kuseri kwa chipilala. Aja achidwi, pamene adagogoda adaona nthawi yomweyo (pompo) chitseko chidatsekuka; nkhope ya munthu wamayi idaoneka. Munthu wamayiyo adali wachitsikana, wowala ngati nyenyezi, wokongola kwabasi. Iye adawalozera ku tebulo lodyera. Ali konko operekera zakudya adabwera nazo; atsikana awiri ovala bwino kwabasi. Akudya adawapatsa vinyo m'tizikho tabwino ta chikhudu. Akuti azimwa adangoona munthu wamayi uja watenga kandodo kake. Atamenya nako aliyense pa mutu, onse adasandukiratu nkhumba. Uja adabisalayu pomvetsera adamva nkhumba zikudzuma m'katimo. Poti amvetsere ndithu adamva nkhumba zikudzuma modandaula.

[10.06]

Munthu ameneyu, misozi idamgwera nisambitsa nkhope yake yonse. Liwiro lokhalokha, adanka nalira kwa anzake aja adatsala ndi **Bwampini**. Pomuona anzakewo maso atatupa ndi kulira, nawonso adayambanso kulira atamva zonse.

[10.07]

'Kwachitikanji?' **Bwampini** adafunsa.

‘Pepani, zachisoni! (*akulira*). Anzathu aja si anthunso, koma asanduka nkhumba.’ Onse adalira kwabasi.

‘Unakapeza ndani?’ ena anzake adafunsa.

‘Munthu wamkazi waukali.’

[10.08]

Pomva zonsezi, **Bwampini** m’chifuwa mwake mudatentha ndi ukali ndi chisoni, adawauza anzake kuti adikire, adzawapeza. Iye ndi maganizo ochuluka adayamba ulendo wake. Nzeru kwenikweni zidamthera, chifukwa iye amapambana anzake onse, koma wamatsenga wotereyu, adayenera kukhala mmodzi wa **Azimu**, koma woyipa. Akatani tsono akakumana ndi mayi wotereyu? Akudzipweteka ndi maganizo amenewa adangoona mwadzidzi [mwadzidzidzi] mnyamata wokongola kwabasi wangoimirira kutsogoloko.

[10.09]

‘Kodi nkwabwino akulu? Nanga ngwakuti umenewu?’ mnyamatayo adafunsa.

‘Ndavutika mnzanu, munthu wamayi wina woyipa mtima wawasandutsa nkhumba anthu anga, nditani pamenepa?’

[10.10]

Mnyamatayo adamuuza kuti adachita zimenezo ndi **Mabuta**, dzina lake lina lachitsikana ndi **Namatsenga**. Munthu wamkazi wokhwima kwabasi. Adamulozera chitsamba china, namuuza kuti ngati iye akalandire chakumwa chilichonse ndi chakudya chomwe, akatafunire muzu wachitsambacho.

[10.11]

Iye adalandira mothokoza, nayenda ndawala. Atafika pakhomo la nyumba adagogoda, namtsekulira. Adaona munthu wamkazi watimaso tonyenga ndi taumambala. Adampatsa moni, namulozera kumpando wa kutebulo. Kumeneko adapeza chakudya choperekedwa ndi atsikana omwe aja. Vinyonso adaperekedwa. Iye adakumbuka mawu a **Mapiko**, mnyamata wokongola uja, nayamba kutafunira mtengo uja. Munthu wamkazi uja adanyamuka namumenya pa mutu. Ngwindiri! Chosasanduka chilombo!

[10.12]

'Ndiwedi munthu wobadwa ku **Sachokeka**?'

'Ndine, umatinji nanga?' Poyankha tero, **Bwampini** adatenga lupanga lake m'chimake nafuna kudula mutu wa mfitiyo.

'Chonde usandiphe! Chonde usandiphe!' adalira **Namatsenga**. Pompo iye adakumbukira mawu a mneneri wina amene adamchenjeza za mlendo wina dzina lake **Bwampini**. 'Kodi ndinu **Bwampini** kapena?'

'Ndine, chiyani! Ndikupha lero, ukapanda kundipatsa anthu anga. Fulumiza asandulitse anthu.'

'Musandandaule [Musadandaule], abwera tsopano apa,' adatero mayiyu. Pomva kuzaza kotero, **Namatsenga** adachita mantha nakasandutsa anthu nkhumba zija.

[10.13]

Posachedwa adaona anthu akubwera. Iye adathunthumira nawapatsa moni wachanza. Adafuna kulawira kwa **Namatsenga**, koma **Namatsenga**yo adawapempha kuti akhale pansi ayambe acheza pang'ono.

[10.14]

‘Ukufunanso kuti tonsefe tisanduke nkhumba?’ **Bwampini** adakana.

[10.15]

Koma **Namatsenga** adagwetsa nkhope ndi chisoni ndi manyazi, napepesa chifukwa cha chipongwe chake. Ndipo adapempha **Bwampini** kuti akhulule namuuza kuti zonse zatha, ayiwale pochita phwando. Apo onsewo adamvana.

[10.16]

**Namatsenga** adatuma mthenga kukaitana otsalira. Atafika onse akale ndi atsopano adawauza kukasamba madzi ofunda. Atasamba adawalozera chipinda china kumeneko adadzola zonunkhira, kupesa bwino ndikuvala zosita ndiponso zatsopano. Anthu amakongola ndi madzi ndi zovala. Potuluka umo **Bwampini** nkuti atasanduka wokongoladi. Ena nawo adaoneka a nkhope zachinyamata ndiponso okongola. **Namatsenga** naye, adali payekha. Atumiki akenso chimodzimodzi.

[10.17]

Chaka chidagundika. Mikate yophikidwa bwino, nyama yamtundumtundu, zipatso, vinyo wonunkhira yekhayekha. Nyimbo zili m’kati, chifukwa **Namatsenga** adali ndi amisiri ambiri a nyimbo, anthu adadya ndi kumwa koyiwala nako zonse. **Muvina** adagwira mngoli wake, nayimba za ulendo wa **Angitau** ku **Gangire** ndi nkhondo yawo yonse. Apo anyamata adalira pomva za masautso awo, kwinaku chimwemwe, chifukwa mmisiriyo adayimbanso za tsiku limene **Zimeze** adalowa ufumu.

[10.18]

**Namatsenga** adadoma ndi umisiri wotero wa nyimbo. Pompo adamufupa mkanjo wa golide mmisiriyo.

[10.19]

Onse atadya ndi kukondwa choncho, **Bwampini** adadzuka ndikuthokoza mayi waufuluyo; namudziwitsa kuti nthawi yoyambanso ulendo yakwana. **Mabuta** adamva chisoni navomereza. Adauza atumiki kuti abwere ndi chakudya ndi chakumwa kuti alendo anyamule. Adawapatsanso aliyense wa iwo zovala zambiri. Iwo adanyamuka ulendo wakugombe. Atafika adakokera ngalawa m'madzi, nauyambanso ulendo.

**Mutu 11**

**Namondwe woopsa**

[11.01]

Anthu onse mitima idali m'malo, angakhale ena mwa iwo adakulawa kukhala nkhumba, koma izi zidapsinjidwa ndi mphatso ndi ufulu womwe adaulandira kwa **Namatsenga**. Ali waliwali m'zovala zochititsadi kaso, sadaganizenso zina koma kuvina, kudya, kumwa ndi nkhani basi.

[11.02]

Uli mkati ulendo kutali kudamveka zitoliro, malipenga ndi ng'oma, ndipo kudamveka nyimbo zimene **Muvina** adachita nazo chidwi. **Bwampini** nayenso adazimva. Poganiza adakumbukira zimene adazimva kwa mnzake wina pocheza. Mnzakeyo adati, mbali ina yakumpoto kwa dziko la **Ngitau** kudali mtundu wa anthu akuluakulu, amiyendo ngati ya mbalame ndi zikhadabo zomwe, koma odya anzawo. Anthuwa amapusitsa ena powaitana ndi nyimbo zokoma. Pomwepo adakumbukira kuti anthu ambiri adaphedwa posachenjera.

[11.03]

Kwenikweni padalibe mankhwala enieni koma kumata phula mkhutu. Zisadawathere nyimbozo, **Bwampini** adawafotokozera izi anzake, nawapempha kuti onse amatane phula mumakutu. Iyeyo, **Bwampini**, adapempha kuti asamumate phula m'makutu, koma kuti amumangirire ku ngalawayo.

[11.04]

Izi zidachitika. Akuyenda choncho pamodzi adasendezera pafupi ndi nyimbo zokomazo. Popeza makutu adatsekeka ndi phula, amalinyero adali ngati agonthi, ngakhale nyimbo zotsekemerazo adazikweza ndi kuzikometsera kopambana, koma iwo sadasamare, ndipo iwo adangopalasa kwambiri. Mpweya wonse udadzadza ndi nyimbo zokomazo. **Bwampini** adafuna kudzimasula kuti akaone ndimaso ndi kumva zokoma zimene zidali kuyimbidwa, komanso anthu oyimbawo anali ndani?

[11.05]

'Ndimasuleni chonde!' **Bwampini** adapempha, koma padalibe woti amumasule. Mwamwayi adapapitirira. Kenaka adamumasula namuyamika chifukwa cha nzeru zake.

[11.06]

Ulendo udali pafupi kumapeto. **Muvina** adagwira mngoli wake nawakumbutsa za chaka chachikulu kunyumba ya **Namatsenga**. Adayimbanso nyimbo yokumbutsa zakubadwa kwake kwa mfumu **Zimeze**, mmene anthu adakondwerera. Onse nkhope zawo zidawaladi ndi chimwemwe.

[11.07]

Zimenezi zikuchitika, adangoona **Ndomondo** bambo wa **Chikutumbwe**, ndipo nthawi yomweyo adatuma mphepo yoopsa imene idautsa mafunde akuluakulu. Kudachitika chinamondwe. Madzi adazaza [adadzadza] koopsa. Ngalawa ziwiri zidapita uku ndipo anthu m'katimo adatayidwanso uku ndi uku. Mitima idangoti myuu! nthawi imodzi.

[11.08]

‘Gwiritsa!’ adapfuula **Bwampini** kuchenjeza anzake. Onse adadziwa kuti **Azimu** awakwiyira, makamaka **Ndomondo**. **Chikutumbwe** adanenadi zoona, koma adakatani nanga? Ngalawa ziwiri zonse zidanyamulidwa m’mwamba, mmene zinkagwa pansi, zonse zinaswekeratu.

[11.09]

Onse adamiriratu, ena kungoti balala ziwalo kutayana. Onse adaferatu kupatula **Bwampini** yekha, yemwe adaumirira kwathunthu thabwa limene lidali kuyandamabe. Nkhope yake idatupa ndipo thupi lonse lidali lopweteka ndithu. Sakanatha kuchita chilichonse, nzeru zinamuthera. Iyeyo anangonka nalo thabwa kulikonse kumene linali kuyandama.

**Mutu 12**

**Gingiswa**

[12.01]

Pagombe pena panali kukhala mkazi wina, amene **Tinjiwa** adamuchotsa muufumu wake ku **Ntheradi**. Dzina lake **Gingiswa**. Iye anali kukhala yekhayekha m’phanga, koma lokongola koopsa. Apo ndi apo timaluwa, tizithunzi tolemba yekha, ziwiya zambiri adali nazo. Nthawi zambiri ankakonda kusoka, akati watopa, amayimba mkangala wake, wokongola ndiponso wopangidwa ndi umisiri. Tsiku lina zitamtopetsa zonse, adapita kugombe kukadya mpweya chabe. Atafika kumeneko adadabwa kwambiri.

[12.02]

Adaona munthu wamamuna wokongola ali mtulo. Iye sadamvetse kuti adabwera bwanji? Atamuyang’anitsitsa nawona kuti nkhope yake idali yotupa, thupi lake apa ndi apa litasendeka, zovala zake zitang’ambikang’ambika ndi kudzadza ndi zitsotso ndi

udzu wa m’madzi. Adamgwedeza munthuyo sadadzuke, koma anali asanafe, chifukwa anali kupumabe.

[12.03]

Popeza kuti **Bwampini** anali ataonda kwambiri ndi zovuta zonse adakumana nazo, iye adapepuka kwabasi, kotero kuti **Gingiswa** sadavutike pomunyamula. Atafika naye kwawo, adamgoneka pamalo abwino namfunditsa nsalu ndi bulangeti. Pomva kutentha pang’ono, iye adapenya pang’ono, kodwala kupenya kwake, nazindikira kuti anali m’nyumba mwa mwini wake. Poona zimenezi, **Gingiswa** adamudzutsa nampempha kuti akasambe. Atasamba ndikudzola zonunkhira, **Gingiswa** adampatsa zovala zonyezimira kuti avale. Iye atavala ndi kusinthika, ngakhale adali chifookere.

[12.04]

**Gingiswa** adamusirira kwabasi, mumtima mwake naganiza kuti akadapeza danga lokwatiwa, koma izi adazibisa mumtima mwake. Atakonza chakudya chonunkhira ndi chakumwa choyenera, **Gingiswa**, mwaumisiri wake wonse, adapempha **Bwampini** kuti asendezere pafupi. Nkhani imodziimodzi idasweka pamenepo. Ayi, padalidi kucheza, kudya ndi kumwa komwe. Apo adapeza mwayi wompatsa moni ndi kumfunsa kumene akuchokera.

[12.05]

**Bwampini** adafotokoza mwatsatanetsatane. Kwawo kudali kwa **Angitau**, kumene adachokera, ndi mfumu **Zimeze** kukamenya nkhondo ku **Gangire**. Konko adachoka ndi anyamata ake ochuluka kubwerera kwawo, koma adasiyana mnjira ndi anzake ena onse. Adatsindika kuti adawona masoka ambirimbiri, ndipo anzake ambiri adapeza tsoka lokhalokha: ena adaphedwa ndi njoka, ena **anyani-anthu** [**Anyani-anthu**], ena ndi chikutumbwe [**Chikutumbwe**]. Ambiri amene adali nawo adatayika m’**nyanja** [**Nyanja**]. Tsopano iye yekha watsala wopanda mnzake ndi mmodzi yemwe, ndipo adataya chikhulupiriro chokaonanso kwawo.

[12.06]

**Gingiswa** adamvetsera ndi chidwi chambiri, nkhani yokoma koma yomvetsa chisoniyo. Adampepesa **Bwampini**, namuuza kuti mwina adzachita mwayi nakafika kwawo. Kunali kutada, tsono iwo onse adakagona aliyense payekha.

[12.07]

Kutacha, **Gingiswa** adadzuka mwamsanga ndi kukonza madzi, kuphika chakudya chammawa monga momwe amachitira atsikana ndi azimayi achangu a m'mabanja. **Bwampini** atadzuka adakasamba kuchipinda chosambira ndikubwerera atasanduka wina. **Gingiswa** adamuitanira ku tebulo nayambanso kudya.

[12.08]

Nthawiyi **Bwampini** sadadye ndi nsangala. Adakumbukira zoipa zimene adaziona, natsimikiza kuti kufa panthawi yamasautso oterewa ndi kwabwino kwabasi. **Gingiswa** adazindikira msanga kuti mnzakeyo adali ndi chisoni chachikulu. Achikhala munthu chabe chisonicho chikadamupha **Bwampini**, koma anthu anzeru, imfa, mwano, tsoka, zonsezi siziwatayitsa mtima. Tsono adamva ululu mu mtima mwake umene sitingathe kuufotokoza.

[12.09]

Munthu wamkaziyo adayesa kugwira mkangala wake ndikuyimba nyimbo zosangalatsa moyo, koma sadathe kukondweretsa **Bwampini**. Adayesa kumuyimbira ndi liwu lake lokongola, lopambana mkangala umene anali kuyimbawo, koma adalepherabe. **Bwampini** adapempha munthu wamkaziyo kuti akagone ndipo adakagona chifukwa m'thupi mudali kumpweteka. Patapita nthawi **Bwampini** adapeza mphamvu zake, zilonda ndikuwawa kulikonse kwa m'thupi kudaleka, koma chisoni chidadya mtima wake ndi kumulumaluma tsiku ndi tsiku. **Gingiswa** adalephera kupeza njira yomkondweretsa.

[12.10]

Nthawi zambiri **Bwampini** ankakonda kupita ku gombe la**nyanja** [**Nyanja**] ndi kuganiza zakwawo. Ankakonda kuganiza za **Angitau** onse, **Zimeze**, nkhondo yaikulu ya ku **Huwa**. Poganiza zimene zidachitikira anzake aulendo nthawi zonse iye anali kulira. Chisoni chidamgwira kwambiri pamene adaganiza za mkazake **Namasinkho**. Panali patapita zaka makumi awiri. Mkazake adamusiya akadali namwali. Kodi iyeyo sakampeza atakwatiwa ndi asatana ena?

[12.11]

Kalekale mkazi wake pamene adali buthu adaonetsa chikhalidwe chokoma, ngakhale mmene adakula chinamwali, nakhala mbeta, makhalidwe ake adakomerakomera. Kaya popeza kuti akazi nthawi zina sakhulupirika. Zakuseri sungadziwe.

[12.12]

Akuganiza zimenezi, **Gingiswa** adabwera ndi chifundo chocheza naye. Nkhani zidali kuyenda ndithu. Kenaka adamuuza **Bwampini** kuti asamalote zakwawo. Mkazi wampeza kale angokwatira basi. 'Kapena sufuna kukwatira mtsikana wa **Chizimu**?' **Gingiswa** adafunsa. Ponena zoona, **Gingiswa**yo adali wokongola kwambiri ngakhale **Namadanitsa** yemwe sakadafola naye. Padalibiretu ku **Sachokeka** mkazi wokongola kuposa **Gingiswa**. Ngakhale **Namasinkho** pokongola akadatha kulowamo mwa **Gingiswa**, makumi okhaokha khumi, ngakhale kupambana pamenepo.

[12.13]

**Bwampini** adati kwa **Gingiswa**, 'Tamvetserani. Mungakongole, mungadiuzenso kuti ndikakukwatirani sindidzafa? sindingatero. Ine ndine wa ku **Sachokeka**, ndipo ndidzakwatira wa ku **Sachokeka**. Ndiponsotu mukungovutika, ndili naye kale mkazanga, **Namasinkho**. Pano akungondididikira.'

[12.14]

Ngakhale kuyankha kotereku kudali kwa mwano, **Gingiswa** sadalekebe kumpempha kuti angokwatirana, ndipo **Bwampini** adapitiriza kumakana. Masiku ambiri **Bwampini** adakhalira kulira ndi kudandaula.

[12.15]

**Tinjiwa** ataona izi, iye adatuma **Mapiko** kuti adzamuuze **Gingiswa** amuleke **Bwampini** azipita kwawo. Kachidzulo, **Bwampini** ali pagombe, **Mapiko** adamuwonekera **Gingiswa** ndikumuuza uthenga wa ku **Ntheradi**.

[12.16]

'Kodi chifukwa chiyani **Tinjiwa** ndi ena nonsenu mumangondilondalonda? Mudandipitikitsa kale osangondisiya? Ndisiyeni ndizichita zofuna zanga!' adandaula nalira **Gingiswa**.

'Musadandaule si ndine ndikunena izi. Inu mungomvera, chifukwa mukakana mutha kupeza nazo zovuta.' Atanena zimenezo **Mapiko** anachoka. Atafika **Bwampini**, **Gingiswa** adamuuza kuti tsopano atha kukonzekera kupita kwawo.

[12.17]

Apo m'mphawiyu adakondwera ngakhale adada nkhawa ndi ulendo wa munthu mmodzi. **Gingiswa** adamubwereka nkhwangwa, ndi zida zosemera bwato. Ndi chimwemwe chodzadza tsaya **Bwampini** adaphotchola patchire, naona chimtengo chachikulu, nachigwetsa. Ntchito idayambika yosema bwato kenaka natsiriza.

[12.18]

**Gingiswa**, ngakhale mosakondwa, adam'patsa chakudya, chakumwa, zovala ndi mphatso zambiri, namperekeza kugombe. Atalawirana, **Bwampini** mwa msangamsanga adanyamuka ulendo wayekha kunka kwawo.

[12.19]

**Tinjiwa** adaona **Bwampini** namumvera chisoni. Adatuma **Mapiko** kuti amperekeze mpaka kudziko lakwawo. **Mapiko** adanyamula mphatso zokafupa kupirira kwa **Bwampini** ndikulimba mtima kwake. Mphatsozo zidachokera kwa **Azimu** osiyanasiyana a ku **Ntheradi**.

**Mutu 13**

**Mbalame ibwerera ku Chisa I**

[13.01]

Nyumba ya **Bwampini** idali pakati pa mapiri a ang'onang'ono. Nyumba yachifumuyi idali yayikulu ndiponso yokongola kwambiri. Mfumu idali ndi atumiki ambiri, aakazi ndi aamuna omwe, ngakhale ena adasiya ntchito poona kuti mwini nyumba sakubwera.

[13.02]

Pamene mwamuna wake ankapita ku nkhondo, **Namasinkho** adali wodwala. Patapita nthawi pang'ono adabereka mwana wamphongo, namutcha dzina loti **Uziona**, pofuna kutanthauza kuti adabadwa nthawi ya zoopsa. Mkaziyo, chichokere mwamuna wake kukongola kwake kudali chikhalire. Womuona ankangoti ndi namwalibe koma ai. Poona nthawi ikukula, chisoni chidayamba kukulirakulirabe, nayamba kuganiza kuti mwina mwamuna wake adaphedwa panjira. **Uziona** nayenso adakula ndi kukhala mnyamata wamkulu. Iye ankadziwa kuti abambo ake adapita kukamenya nkhondo kalekale ndipo ankakhulupilirabe kuti adzabwerera.

[13.03]

Anthu a ku **Buwa** adatopa ndikudikira mfumu yawo. Pamene zidatha zaka khumi, ambiri a iwo adakhulupirira kuti **Bwampini** mfumu yawo siidzabwereranso. Pa chifukwachi

ambiri mwa iwo adayamba kunyalanyaza. Ambiri mwa iwo sadalabadire za malamulo ena, angakhale padali nduna ndi makosana ogwirizira mpando, podikira kuti **Uziona** akhwime. Choncho amuna ambiri, okongola, amawoneka achifumu, ena ochokera kumayiko osiyansiyana adadza ku nyumba kwa **Bwampini**. Adabwera ndi chuma ndi zina ndi zina kuti adzanyengerere **Namasinkho** ukwati. Onsewo ankalakalaka kwambiri kuti amukwatire. Iye ngakhale anali kukana, koma iwowa ankamukakamizabe.

[13.04]

Choncho m'nyumba ya mfumu simunkachoka alendo. Alendowa anali kudya chakudya cha m'nyumbamo; nyama ya nkhumba, mbuzi, ng'ombe, nkhosa, nkhuku ndi mpunga. Zipatso za mitundumitundu, vinyo wonunkhira osalephera. Zimenezi zinkachitika tsiku ndi tsiku, kotero kuti chakudya ndi chuma cha **Bwampini** chidali kutha pang'onopang'ono, ngakhale chidali chambiri.

[13.05]

Masewera amtundu uli wonse ankachita m'katimo, ambiri oledzera ankangochita phokoso, kutukwana, mwina kumenyana ndi kusakaza ziwiya za m'nyumbamo. Makosana ndi nduna zazikulu za ku **Buwa** zidadziwitsa amunawo kuti ngati ankafuna chikwati ankayenera kuchita zonse mwaulemu, osaononga chuma cha mwini. Koma iwo ankangotsonya ndikutsira kunkhongo.

[13.06]

Anthu onse machitidwe amene ankachita m'nyumba mwa mfumu **Bwampini** sadawakonde. Ambiri adasirira ndikupempha kuti anthu a ku **Ntheradi**, makamaka **Tinjiwa** akadabwera ndikuthetsa zachipongwezo.

[13.07]

**Namasinkho** nayenso chipongwe cha amunawo chidamzulo moyo kwambiri. Poona ziwiya ndi mipando, zonse zikuwonongeka m'nyumba mwake, adalira kwambiri mosisima m'chipinda mwake.

[13.08]

Tsiku lina amunawo akudya, ena mwa iwo ataledzera kale, iye adachoka kuchipinda chake nabwera kumene anali kudyerako, naima pamakwerero nati, 'Mukundimvetsa chisoni kwambiri, poti ngakhale mwabwerera ine, mukongosakaza katundu ndi ziwiya. Mwana wanga mukumuthera katundu ngakhale mungoti mudzabwezera. Mwabwerere chikwati, komatu ine ndekha mundilephera, nonsenu yakusiyani sitima. Mukhaula!' Atatero adatuluka.

[13.09]

Ofuna chikwatiwo, izi sadapse nazo mtima, koma adangoseka. Mkulu wawo, **Phakaphaka**, adawalimbitsa mtima nati, 'Nonsenu muno musataye mtima. Kodi simudziwa mmene akhalira anthu a akazi? Safuna kulola munthu kuyambankuyamba. Nzeru zawo nthawi zonse ndi kunyengezera kukana basi. Chitsiru chokha chimataya mtima msanga mtsikana akamati, "Toto ine, toto." Mawamawali, mayiyu timpanikiza mpaka atiuze zakukhosi kwake. Tidzamfunsa kuti atiuzitse. Nkotheka kusankhula mmodzi mwa ife. Akadzakana tidzayeneradi kuyisiya nyumba ino ndikumulekera chuma chake. **Uziona**, mphwanga akumva apayo.'

[13.10]

Atatero onse adamuombera m'manja ndipo pompo **Phakaphaka** adayitanitsa chakudya ndi chakumwa chonunkhira. Padalidi kudya ndi kumwa ndi kusewera kwambiri. Chiphokoso chidakula ndikuseka. Anthu apanja zidawawawa mtima, chifukwa anthu oipawo adali kutha chuma chamwini. Chaka chiri mkati, **Uziona** anali nawo pa phwandoli, ndipo zimamuwawa kwambirimbiri zimene zinali kuchitikazo, koma sadaonetse pankhope yake.

[13.11]

**Tinjiwa** adamumvera chisoni **Uziona** namtumizira mthenga wamkazi. Anthu onse akudya, **Uziona** adaona mkazi wokongola, atavala zonyezimira kwambiri. Ena onse sadamuone. Dzina lake **Ching'aning'ani**.

[13.12]

Atapatsana moni wa ku **Ntheradi** adati, 'Ndatumidwa ndi bambo anga **Tinjiwa**, kudzakudziwitsa kuti udziwe kuti bambo wako sadafe akadali moyo. Iyeyo ali munjira. Mawamawali mudzawaonana [mudzawaona, mudzaonana] ndipo mwezi womwe uno adzalowa muufumu wake. Iwetu tsono izi udziwe ndi mtima wako basi, osawuza wina aliyense. Ukadzaona mlendo wadazi ndi makwinya usadzamupitikitse. Ndapita.'

[13.13]

Kuyambira pamenepa **Uziona** mtima wake ngati uphulike ndi chimwemwe, ngakhale sadathe kuchigawirako wina aliyense, ndi mayi wake yemwe. Pompo adayitanitsa chakudya ndi chakumwa. Kenaka adapita apa ndi apo nacheza ndi kusewera ndi alendowa angakhale adali adani ake.

[13.14]

**Phakaphaka** yemwe adali kusakaza nawo chuma cha **Bwampini**, adadabwa ndithu ndi **Uziona**, wosamvetsa chimene chidamukondwetsa popeza kuti nthawi zambiri, iyeyo akangodya [ankangodya] ndi kumwa pang'ono ndiponso osasangalala kwenikweni.

[13.15]

'Mwakondwatu lero abwana, kodi kwatani? Ndi a **Uziona** omwe lero kuledzera?' adadabwa **Phakaphaka**.

**Uziona** adamuyankha mwaulemu, ‘Kumakondwa nthawi zina, ndiye tizingofa ndi chisoni tikamangomva kuti tiribe atate athu. Kumaiwala nthawi zina.’

‘Kani ukadakhulupirirabe kuti atate wako adzabwera?’ **Phakaphaka** adadzidzimuka. ‘Iwe pa zaka makumi awiri osataya mtima! Ndidamva mnzanga wina, koma ameneyo sanama nthawi zambiri, adandiuza kuti atate wako adaphedwa ndi namondwe. Tsono ndi bwino kungoyiwala.’

‘Aaah! Ngati ndi choncho ndiyenera kuyamba kukhuza maliro tsopano,’ adatero **Uziona** ndi liwu la chisoni.

**Mutu 14**

**Mbalame ibwerera ku Chisa II**

[14.01]

**Mapiko** ndi ku **Ntheradi** komwe adali ndi nkhani zambiri. Akakhala pakati pa **Azimu** anzake ankangokhalira kuwaseketsa. Poona kuti **Bwampini** adali ndi chisoni chambiri, adayesetsa kuti amuiwalitse zonsezo. Adamukambira nkhani zosiyanasiyana. Poyamba adamukambira nkhani yachisoni ya mfumu **Zimeze** amene adaphedwa. Pofunsitsa **Bwampini** adamva kuti mfumuyo posadziwa kanthu za zimene zidali kuchitika m’nyumba mwake, mmene idatha nkhondo ija, iye adafuna kulowa m’nyumba mwake, koma pakhomo adakomana [adakumana] ndi munthu amene amanyengana ndi mkazake, **Nachimasomaso**. Munthuyo adali ndi nkhwanga m’manja, adayiponya m’mwamba ndi kuzula nayo mutu wa mfumu **Zimeze**. Izi zidali zopangana munthu wadamayo ndi **Nachimasomaso**.

[14.02]

**Bwampini** adamva chisoni kwambiri chifukwa mfumu **Zimeze** adali munthu wabwino kwambiri, koma iye adachita tsoka kukwatira mkazi woteroyo. Ndi kale lonse **Nachimasomaso** akadali namwali ankasewera ndi mnyamata aliyense, mwina kuwatsekulira amuna. Mfumu **Zimeze** ngakhale idali mfumu yokoma mtima, pamodzi

pokhapo idalephera posamvera akuluakulu akumuuza kuti namwaliyo adali chidzete, eedi, chidenterinte, chitsime cha aliyense.

[14.03]

Ngakhale zinthu zidayenda choncho, **Bwampini** adayamba kufuna kutemberera mtundu wonse wa azimayi, nati munthu wamkazi mtima wake udali wolefuka, wosakhalira kunyengedwa, ndiponso wopanda chipangano!

[14.04]

Apo adatsutsana ndi **Mapiko** kwabasi amene adati alipo akazi ena adama lamsala, ochita kuthamangira amuna, ochita kuwalira ndi kuwatsekulira amuna, mwina ndi tiana tomwe. Koma ena alipo osunga chipangano, akhalidwe losagwedezeka, atsikana enieni angwiro ongofuna chikwati, banja basi!

[14.05]

**Mapiko** adapitiriza kumuuza mnzakeyo kuti kawirikawiri amuna amalakwa ponyengezera kuti akazi okha ndiwo ali ndi **chimasomaso** [cf. **Nachimasomaso**], apo pokha ndiye bodza. Alipo inde amuna ena okhulupirika kwambiri, koma enanso alipo amene amangokonda kusudzulasudzula, kukwatira apa ndi apa, kuthamangathamanga ndi munthu wa mayi aliyense. Anthu otere sasankha, amangogwira m'khosi aliyense, mwina ndi **Nalitsiro** yemwe, **Nasasamba**, **Namamina**!

[14.06]

**Bwampini** adadala, mnzakeyo adatero, chifukwa **Namasinkho** ndiye adapambana azimayi ndi atsikana onse polewa ndikupirira zadama. Anthu ambiri adagwa dala m'milandu chifukwa chosafuna kupewa zonyenga ndi misampha yonse. Akucheza tero, ngalawa inali kutha mtunda wa m'madzi. Mapiri a ku **Buwa** adayamba kuonekera.

[14.07]

**Bwampini** pomva nkhani za mnzakeyo adakondwa kwambiri, chifukwa mumtima mwake anali kupeneka za mkazake. Iye anali kukhulupirira kuti anthu akazi amangofuna kusinthasintha amuna ngati duku!

[14.08]

Adadaladi **Bwampini**. **Mapiko** adapitiriza, chifukwa pa zaka makumi awiri, **Namasinkho** akadakhala mkazi wina, bwenzi atakwatiwa kalekale, mwina nakhala ndi zidzukulu. Koma **Namasinkho** sadatero ndipo anali kudikirabe mwamuna wake.

[14.09]

'Kunyumba kwanga kuli bwino?' **Bwampini** adafunsa ndi nkhawa.

[14.10]

**Mapiko** adafotokozera mnzakeyo kuti kunyumba kwake, sikunali bwino kwenikweni. Kudali amuna ambiri ofuna kufunsira mkazake koma iye anali kukanitsitsa. Chakudya ndi chuma ndi zomwe zidali pafupi kutha. Zonse zinali pwirikiti. Kunali kofunika tsono kuti pokafika kunyumbako akachenjere kwabasi.

[14.11]

Adamdziwitsanso kuti sadayenere kuopa chifukwa **Tinjiwa** adalonjeza kumuteteza kwa adani ake. Iye **Mapiko** adabwera kudzamthandiza mpaka atafika pa khomo pake. Adamziwitsanso kuti kudabadwa mwana wa mwamuna nthawi imene adangochoka kupita ku nkhondo, dzina lake **Uziona**, amene tsopano lino anali munthu ndithu wa**msinkhu** [cf. **Namasinkhu**].

[14.12]

Pomva izi **Bwampini** adakondwa kwabasi. Ngakhale adapeza zovuta zochuluka m'moyo wake, koma zidaliponso zokoma. Kubadwa kwa **Uziona** kudali chimodzi mwa zinthu zokomazo. Ngalawa idali pafupi ndi gombe la ku **Buwa**. Atakocheza adatulutsa katundu yense mbwato, ndi kumuuunjika pabwino. Chidalidi chikatundu, chuma choposa chuma chake chakale, ngakhale mfumu **Zimeze** adalibe chuma chotero, chifukwa zambiri zidali mphatso za **Tinjiwa**.

[14.13]

Atatulutsa katundu yense **Mapiko** adauza mnzakeyo kuti apangane za kayendedwe. Katundu adayamba wabisa. Adamuuza kuti tsopano sibwino kuti anthu adziwe zakubwera kwake. Kotero **Bwampini** adayenera kusanduka nkhalamba. **Mapiko** adasanduka mnyamata wa ku **Buwa**.

[14.14]

Pompo onse adasandukadi! Wina nkhalamba ya makwinya, wina mnyamata. Adaperekezana ku nyumba kwa **Bwampini**. Asanafike adangomva phokoso la anthu oledzera ndi otupidwa. Nkhalamba ija sidamve bwino poona ndi kumva zotero. Onse adayenda ndi kufika pa khomo. Atatero adagogoda. Woyamba kutsekula adali **Uziona**. Adaona mnyamata ndi nkhalamba ya makwinya. Poona izo adakumbuka mawu a **Ching'aning'ani**, kotero nthawi yomweyo adazindikira kuti atate wake wabwera ku **Buwa**.

[14.15]

Onse adali pakati pa chaka, zakudya ndi zakumwa zonunkhira kwabasi zinkangobwera. **Uziona** adaitanitsa mbale kuti adyeremo alendo, koma akuluakulu ena sadasangalale nazo zimenezo. Zitsirunso zinali kudya nawo chakudya choyenera ana a mafumu. **Bwampini** adadya ndi kumwa mwamantha. Poyang'ana pabwalo kudaoneka kuti kunjako kunada, anthu m'kati mwa nyumba adavina, kudya, kumwa ndi kusewera.

Kunali kutada ofuna kugona adapita kukagona. **Bwampini** adapempha malo ogona ndi mnzake, **Mapiko**. Zonse zimene adapempha adalandira ndikupita kukagona ndi tcheru.

**Mutu 15**

**Mbamba ndi ching'aning'ani [Ching'aning'ani]**

[15.01]

Usiku wa dzulo maloto adapha **Namasinkho** kwabasi. Adalota amuna awo atabwera. M'mawa atadzuka mphamvu zidamthera, ndipo thupi lonse lidali lolefuka kwabasi. Mphamvu adalibe. Kodi adalotadi zoona? Kutacha **Bwampini** atabwera ngati dzulo lake, ndi **Mapiko**, anthu onse mitima inali thithithi ku **Buwa**, kugunda kwabasi. Kumwamba kudagundika zigugululu, mbamba ndi zing'aning'ani, koma chikhalire kudali dzuwa loopsa. Mantha aakulu adagwira nkhalamba, ntchembere, atsikana, anyamata, nkhosa, mbuzi, ng'ombe, nkhuku, mbalame, zilombo zonse za m'madzi ndi za pa mtunda zomwe.

[15.02]

Amuna aja amene ankafuna chikwati ndi **Namasinkho**, adachita mantha nawo, koma sadaleke kudya ndi kumwa nthawi itakwana yodyera chakudya cham'mawa. **Bwampini** poti adauzidwa kale ndi bwenzi lake, **Mapiko**, zamwambo wa tsikuli, adamvetsa ndi kumuuza mwana wake, **Uziona**, ngakhale adali asanadziwe kwenikweni, kuti tsikulo lidali tsiku la chilungamo.

[15.03]

**Tinjiwa** adatuma **Mziisi**, **Mbamba** ndi **Ching'aning'ani** kukalanga amuna achipongwe ndi akhwinthiwo amene anali kutha chuma chamwini.

[15.04]

Oyang'anitsitsa kumwamba, ku **Ntheradi**, adaona mbalame zitatu zazikuluzikulu ngati agalu, zikubwera kuchokera kutali. Amakutu nawo adamva ngati chimkokomo chachikulu champhepo, phokoso la zigugululu, mphenzi ndi zing'aning'ani zidankirankira. Anthu anzeru adamvetsa kuti **Azimu** amafuna kulanga dziko la **Buwa**, koma sadadziwe chifukwa chake chidali chiyani.

[15.05]

Amene anali kudya aja adayamba alekeza kudya, chifukwa cha mantha. Ena adati ayeserebe kudya koma adapeza kuti anali kuphonya pakamwa ndi manjenje. Kenaka mbalame zija zidatera pa nyumba pa **Bwampini**. Anthu amene adaziona adathawa chifukwa zidabwera ndi ukali. Nthawi yomweyo zidasanduka anthu, akazi awiri ndi mphongo imodzi, onse okhala ndi malupanga.

[15.06]

Mwamsanga zidasowa wosaonekanso ndi maso a umunthu. Onse atatu adalowa m'nyumba muja, koma sadathe kuoneka ndi amuna aja. **Bwampini** ndi **Uziona** ngakhale adali anthu, adawapatsa mphamvu ya kuona ndi maso auzimu pa nthawi yokhayo. **Mbamba** adatseketsa zitseko zonse kolimba kotero kuti padalibe woti nkutha kuthawa; mazeneranso nawo adatsekedwa molimbika. Zonse zitakonzeka, **Mziisi**, mfumu ndi mkulu wa nkhondo, adafuula mwaukali ndi kudzidzimutsa anyamata aja onse ndi mzinda wonse wa **Buwa**.

[15.07]

'Anthu oyipa ndi adyera inu, lero mukhaula, mwasakaza chuma chambiri cha **Bwampini**. Mwamthera chakudya chake; mwavutitsa mkazake, **Namasinkho**. Lerotu mwini wake wafika ali muno koma simunamudziwe! Chifukwa chakupusa kwanuko lero mulandira malipiro a dama lanu ndi misala yanu!'

[15.08]

Pompo zing'aning'ani zidachitikanso, mphenzi ndi mbamba zidabuula koopsa. Nthawi yomweyo, **Mziisi**, **Mbamba** ndi **Ching'aning'ani** adatseteka mitu ya anthu onse aja. Onse adafa!

[15.09]

'Anthu a ku **Buwa**, dzanyamuleni maliro anu, koma musalire, mungaone zoopsa chifukwa imfa imeneyi watumiza ndi **Tinjiwa**. Ana anuwa analibe kukhulupirika, anali achifwamba, oyipa, ndi okakala mitima. Mvetsani, mfumu yanu **Bwampini**, wabwera mu ufumu wake. Lero ali wotanganidwa sikungatheke kumuona koma mawa.'

[15.10]

Mawu ake a mlalikiyo adamveka kwambiri, kotero anthu onse a ku **Buwa** adauzana ndi konong'onezana [kunong'onezana] ndi anzawo nati, 'Ndiye bwino.' Onse adakondwera ndi nkhaniyo. Eni ake a malirowo adabwera kudzatenga maliro a ana awo akusisima. Ena adangowaika chamfupimfupi. Kunalidi maliro ambiri koma osakhuza, osavekedwa ndi kathewera komwe.

[15.11]

Zonse zitakonzeka m'nyumba mwa **Bwampini**, kudamveka nyimbo ndi malipenga oyimba bwino kwabasi. **Chezichezi** adayimba nyimbo ziwiri; yoyamba, yosimba za kuipa kwa anyamata adaphedwawo. Yachiwiri, **Chezichezi** adayimba nyimbo yamaulendo a **Bwampini**, nkhondo ya **Agangire** ndiponso tsoka lililonse limene adalipeza.

[15.12]

Apo onse adamva chisoni ndi kulira naye **Namasinkho** chifukwa cha zovuta zimene mwamuna wake adakumana nazo, komanso onse adakondwera onse [del. onse] kuti mfumu yawo yabwerera ndi moyo. Wokondwa kopambana adali **Namasinkho** ndi **Uziona**. **Bwampini** atakhala pa mpando, chakudya, nyama yonona, idabwera

itakazingidwa bwino. Mpunga ndi chakudya china chonunkhira bwino chidabwera ndipo adadya ndi kumwa. Tsikuli lidali lachimwemwe. Kuseka ndi nkhani zidakula; chimwemwe ndi madalitso adadzadza m'nyumba monse. Atumiki omwe adaledzera ndi kudya kophulika nako, 'Abwera Ambuye tikondwere.'

[15.13]

Kutacha, mafumu ndi anthu adatenga mphatso zamitundumitundu kukaona mfumu yawo. **Bwampini** ndi banja lake podzuka m'mawa adadabwa kwambiri ndi chimpingo cha anthucho. Msangamsanga iye adasamba ndi kuvala monga mfumu **Bwampini**, natuluka panja ndi banja lake. Atangofika pamene anthuwo adasonkhana, ng'oma zidaphulika, m'manja ndipo mudasweka, anthu onse adakuwa ndi kufuula.

'Mfumu **Bwampini** zaka zake zichuluke!'

[15.14]

Pompo ana atatu adaimirira, atavala mochititsa kaso ndithu, nabwera ndi zipukutu zitatu, zamaluwa ofiira, oyera ndi achikasu. Maluwawo adali okongola, ndipo adawapereka kwa mfumu, amene adalandira ndi chimwemwe chachikulu.

[15.15]

Zitatha zonsezi, **Lipenga** wodziwa kuyankhula kopambana, nduna yaikulu ya **Bwampini** idafuula niti, 'Anthu onse lero pokuonani, achita ngati alandira chuma chotayika cha dziko la **Buwa**. Ufumu wanu, nzeru zanu zopanda mnzanu wina womuyerekeza sitidaiwale; mudachoka kalekale anyamata ambiri akumeta ndevuwa tsopano asadayerekeze kubadwa. Anthu onse lero akudabwa ndi bodza la adani anu, amene adalalika ponseponse kuti inu mudafa kalekale. Lero anthu oterowo akuthawa ndipo ena adathawa kale. Pokumbukira masautso anu monga tidawamva dzulo munyimbo ya **Chezichezi** tikulira nanu, makamaka tikupepesani kuti mtima wanu ukhululuke ndi kuiwalako. Landirani timphatso tathu tosakuyeneraniti.' Atatero adapereka kwa mfumuyo: ziwiya zopangidwa ndi luso, nyama zonenepa za moyo, nsalu zolukidwa

bwino ndi amisiri, zopakidwa golide, ndi mmisiri wa ku **Ntheradi**. Apo **Bwampini** adaimirira nayankhula mwachidule:

[15.16]

‘Amayi ndi makosana onse, ndikuthokoza poti mmene ndabwerera kwathumu mwandilandira ndi manja awiri. Mukadakhala ena mukadatha kundikana kuti si ndine **Bwampini**, koma simudatero. Mphatso zanu zionetsa ufulu wanu ndi chikondi chanu kwa mfumu yanu. Sindikukayika konse kuti zonse zidzayenda bwino monga kale. Musamaiwale kuti **Abuwa** nthawi zonse amapambana pa nzeru ndi ufulu kwa alendo ndi kumvana, mtima umenewu musauleke!’

[15.17]

Atatero, **Bwampini** adakhala pansi. Kenaka **Lipenga** adakuwa nati, ‘Masana ano kukhala chaka pafupi ndi nyumba yamfumu ino. Muchite monga **Abuwa** amachitira kukakhala chaka.’ Anthu onse adabalalika ndikukakonzeka. Ena adangofikira kugwira nkhuku ena adabaya nkhumba, ng’ombe ndi mbuzi. Amayi adatanganidwa ndi kuphika. Masana ali pafupi malipenga ndi ng’oma zidalira ku **Buwa**, chaka chidali pafupi. Anthu adayamba kusonkhana. Amayi adabwera ndi chakudya chophikaphika chonunkhira. Onse atasonkhana, akuluakulu, anyamata, atsikana, **Bwampini** ndi banja lake ndiponso iwowa zidakhala malo awo, monga momwe adakonzera.

[15.18]

Anthu adayamba kudya ndi kumwa. Ambiri adaledzera. Anyamata adavina mganda, atsikana adavina likwata ndipo madoda anavina njazo. Anthu anali asanakonzeke kwenikweni ndi zibiya komabe adavina kodabwitsa.

[15.19]

Zamba zidali zambirimbiri, koma chamba chomwe chidamukomera **Bwampini** chidali cha njazo. Akuluakulu omwe adavina chambachi anali kuyimba nyimbo yawo:

[15.20]

‘**Bwampini** mwabwerera, wawa! Kodi nzoona? Tidataya munthu wanzeru zopanda mnzake.

Tidamva za hatchi yanu kwa **Agangire**.

Ulendo wanu wochititsa mantha tikuudziwa:

**Asongo** oluma, **anyani-anthu** [**Anyani-anthu**] adatha anthu athuu, abale athu!

**Chikutumbwe** naye, wamadyo, adaleka mbuzi

Ndi nkhosa, natidyera abale athu.

**Namatsenga** naye kulakalaka, nkusandutsa

Nkhumba abale athu! Nkhanu yolusa

Ndi **amphalusa** [**Amphalusa**], kutithera abale athu.

Namondwe wolusa naye, tidamtani

Ife kuti atitsirizire abale athu.’

[15.21]

Anthu adavina kwambiri, kudya ndi kumwa monga akadathera. Mdima udasakira anthu m’makomo mwawo. Koma atsikana okha nyimbo zawo zidakathera m’makhitchini motere:

[15.22]

‘Mfumu yathu yabwerera, yanzeru kopambanatu.

Ndani timuone woposa **Bwampini**!

Ana aamuna akabadwa, kwawo n’kusauka; inde

Koma kodi, iwe **Buwa**, siuthokoza kuti adakupatsa

Munthu wanzeru, waluso, wakhama, wamphamvu,

Mfumu **Bwampini**?’

**FINIS**